



ZITHUNZI: ESMIE KOMWA

Chadzalema (Pakati) kufotokozera atolankhani mmene mthirirawu udzapindulire alimi

Alimi 223 000 adzapindula ndi mthirira

WOLEMBA:
ESMIE KOMWA

Alimi 223 000 a m'mabanja oposa 48 000 a m'maboma a Chikwawa ndi Nsanje a kuyembekezeka kudzapindula ndi pulojekiti ya mthirira ya Shire Valley Irrigation Project (SVTP).

Katswiri wa zomangamanga ku pulojekiti ya Martin Chidzalema ndi amene adayankhula izi pa m'kumano wa atolankhani umene bungwelo lidachititsa Lachiwiri.

Iwo adati pulojekitiyi imene ikuyembekezeka kudzamatirira malo opitilira mahekitala 43 000 a m'mabomawa zipangizo zonse zothiririra

zikadzamalizidwa kumangidwa ndi kuyamba kugwiritsidwa ntchito.

"Alimiwa abwera pamodzi ngati magulu ndi kuphatikiza minda yawo kuti malo awo akhale aakulu ndi kumadzalima mbewu zochulukana ndi za mtengo wapatali zimene zidzawathandizenso kupeza misika yabwino chifukwa azidzagulitsa ngati gulu ndi kugawana malingana ndi kuchulukana kwa malo a munthu.

"Izi zidzathandiza kutukula alimiwa komanso ngati dziko chifukwa mbewu zimene zizidzalimidwazo zidzakhala zochulukana choncho zidzapeza misika yakunja komanso kugwiritsidwa ntchito kupangira zinthu zina," adatero iwo.

A Chidzalema adati cholinga cha pulojekitiyi ndi kupatutsa madzi kuchoka mu mtsinje wa Shire kupita kuminda kudzera m'ngalande.

Iwo adati m'thirira woterewu ndi wotsika mtengo chifukwa siumadzagwiritsa ntchito magetsi kapena mafuta amene ndi okwera mtengo choncho alimi adzapindula.

"Chimene chidzafunikire ndi kukonza ngalandezi mwina penapake pakaonongeke basi koma sizidzakhala zobooola m'thumba.

"Padakalipano tagwirako gawo la ntchitoyi lokwana 36 pa 100 ndipo bwenzi titapyola apa koma malingana ndi matenda a Covid 19 amene adachititsa

kuti titseke kwa kanthawi tachedwerapo," adatero iwo.

Chidzalema adati makontilakitala omwe akugwira ntchito ali pa kalikili kuti athamangitsane ndi nthawi imene idaikidwa kuti idzakhale itatha alimi ayambe kugwiritsa ntchito.

Pulojekitiyi ndi imodzi mwa ma pulojekiti akuluakulu a boma ndipo cholinga chake ndikuchepetsa mavuto a ng'amba amene madera a m'chigwa cha mtsinje wa Shire amakumana nawo.

Boma la Malawi lidakhazikitsa ntchito za pulojekitiyi m'chaka cha 2020 ndipo ndi pulojekiti ya mthirira yaikululu kwambiri m'dera lino la Africa. ■



Pamene alimi akukonzekera kukolola, ndi nthawi imenenso ayenera kulingalira za matumba amene angasungemo zokolola zawo. Komanso kulingalira za mankhwala kuti zokolola zawo zisaonongeke ndinso kulingalira za kudimba. Mitengoyi idali chonchi pa 29 March 2021:

Matumba osungira chimanga

A makilogalamu 50	Ayambira K90
A makilogalamu 90	Ayambira K300
A makilogalamu 100	Ayambira K350
A makilogalamu 200	Ayambira K400
Matumba a Pics Bags	
A makilogalamu 50	Ayambira K900
A makilogalamu 90	Ayambira K1 200

Zoyanikira chimanga

Za matumba	Zayambira K4 000
Malona	Ayambira K8 500

Zosolera chimanga

Zazing'ono	Zayambira K1 500
Zazikulu (Zopukusa)	Zayambira K19 000
Makina osolera chimanga a dizilo	Ayambira K900 000
Makina osolera chimanga a magetsi	Ayambira K600 000

Mankhwala ophera anankafumbwe

Super Shumba (magalamu 200)	Ayambira K1 350
Actelic Super Dust (magalamu 250)	Ayambira K1 950
Super Guard (magalamu 200)	Ayambira K4 00
Novatelic (magalamu 200)	Ayambira K4 000
Weevil Kill (magalamu 200)	Ayambira K1 150
Ghanrai (mamillilita 200)	Ayambira K2 000
Ghanrai (mamillilita 500)	Ayambira K3 000
Ghanrai (Lita imodzi)	Ayambira K6 000
Cropchem (Lita imodzi 1)	Wayambira K9 500
Mankhwala ophera makoswe	
Ratide (magalamu 100)	Wayambira K1 950
Latex (Magalamu 100g)	Wayambira K800
Rat Guard	Wayambira K500

Mankhwala opha tizilombo ku tomato

Cypermethylene (100ml)	Wayambira K800
Ventum (250ml)	Wayambira K800

Zipangizo zopopera mankhwala ku mbewu

Za malita 16	Zayambira K7 900
Za malita 20	Zayambira K10 000

Feteleza wa madzi wa mbewu za masamba

Multifeed (800g)	Wayambira K4 000
Superfeed (800)	Wayambira K4 000

Mankhwala a nkuku

Lasota womwetsa nkuku 100	Wayambira K700
Hitchner womwetsa nkuku 100	Wayambira K700

Mankhwala opha njoka za m'mimba ku ziweto

Piperazine (30g)	Wayambira K1150
Abendazo (100g)	Wayambira K2000

Tiuzeni umo mitengo ikuyendera kwanuko
potumiza uthenga pa 0888412807